COVID-19: Nthawi zonse satilani uphungu wa boma komanso acitetezo za umoyo.

DIGNITY

Umoyo

Nkhani 12
hello@dignityonline.org.uk
+447340 573 937

Kachisi la Aliyense!

Kulibe akunga ku chikondi cha Mulungu. Kachisi yace ndi ya aliyense. Kulibe kanthu tinali yani kapena tinachita chiani, kuli malo anthu mukachisi la Mulungu.

Kutandalila mudzi kuwela kwa Zambia, ena mwa anzathu anakumana ndi chipembezo cakapatulula. M'malo awo makachisi anali ndi kusankhana. Anali kuzisunga kwa okha ndipo sanafune kali konse kochokela kwa ochedwa 'ochimwa' amaloyo. Chifukwa ca ici, anthu sanamvepo uthenga wabwino. Anzanthu analankhuzana ndi anthu za Yesu, ku masulila kuti Yesu awakonda iwo, kuti anawafera ndipo aliko malo awo mu kachisi. Mayankho anali oziziswa. Awa anthu, mwakabisila, anapita kwa asogoleli akachisi ndi kupempha kuti atengeko mbali mkachisi ponena, "Yesu atikonda ife ndipo afuna ife kubwera ku kachisi!"

Mu Yohane 1:12 Yohane alemba, "Kwa onse ana mulandila iye, kwa onse anakhulupilila pa dzina lache, anawapasa danga lokhala ana a Mulungu." Yohane anena kuti Mulungu ndiwa aliyense ndipo aliyense ali ndi ufulu okhala mbali ya banja lace. Zonse zotupatula, zipisyinjo zonse zili pakati pathu zilibe pindu. Balimbe malo mkachisi la Mulungu. Tonse ndife amodzi mwa Yesu.

Nthawi zina timaweluza anthu, kuti sali ofikapo kugwilitsidwa nchito ndi Mulungu. Pomwe tichita izi tisusana ndi chisomo cha Mulungu. Tiiwalila kuti naife tinali ochimwa ndipo mothalatu tifuna umoyo wa Mulungu. Nichifukwa cache tonsefe tilandilidwe mu Mabungwe Yamoyo ndi mkachisi, ngakhale awo olingalila ife kuti ndife 'ochimwa'. Kulibe munthu aliyense pa thambo ladzikolino omwe Mulungu sanga sewenzetse mnjila yoziziswa ndi mwaulemelelo wache.

Tingathe kuyangananso pa abale ena omwe chikhulupililo cawo cili cosiyanako ndife. Angapite ku makachisi osiyana naife, kupemphera mosiyana kapena kukhulupila nafe mosiyana ndi ife. Mu Chibvumbuluso 7:9, pali chithunzi-thunzi ca Mulungu ca anthu monga "chinyamtindi chachikulu" kuchoka "mdzinda yonse, mtundu, anthu ndi zilankhulo." Pali kutukuka kwa kukulu kwa anthu a Mulungu ndipo tisayembekezele okhulupilila onse kukhala ofanana nafe. Yesu anatiitana ife, kachisi yace, kuti tigwilizane. Tifunika kusimikizila kuti monga okhulupila tiimilile pamodzi ndikupa malo yali yense mu Kachisi yace.

Ziyikeni mu Zocita!

Ganizilani za malo mkhalamo, ndi anthu otani ali osulidwa ndiku chosedwa mkachisi? Ndi anthu ati amene sanamverepo za chikondi cha Yesu? Ndi anthu otani omwe sanga zimve kulandilidwa mu kachisi? Lembeni maina yanthuwo ndipo mwa pempherere. Msabata yosatila, aitaneni kupita nao ku ma Bungwe Lamoyo lanu. Ndipo mcokeko pang'ono mnjira kuti azimve kulandilidwa ndi ku kondedwa.

Pephelani kuti:

1) Mulungu azawaonesa anthu a momwe mwe alili.
2) Mulungu azi kupasani inu danga lo waonetsa chikondi chace.

"Kunali mwamuna, sing'anga, ndipo apishidwa m'mdzi. Ngakhale achipembezo anali ku muopa iye. Ndinlingalila kuti azakhala oyamba kupita kuka mtandalila pomwe tili, ndi mwamuna tilankhulapo. Ndi nalankhuzana naye za Mulungu. Anayamba kulila ndikunena, 'Chinthu cimodzi chondidabwisa ine, ndi anthu kundi opa ine. Aliko anthu akulu akuza kuno kuza lalikila, akulu koposa inu, koma kulibe omwe anali pano kulankhula ndi ine panka pasonga yaine kulila. Mau mwanena kwaine andigwendeza ine.' Mwamuna uyu anatembenukila kwa Mulungju."

- Chafwila, Zambia

Mungafufuze zochuuluka pa:
dignityonline.org.uk/publications

Dignity ndi bungwe ya zaulele yosindikizidwa pa No. 1122656. Dignity (Worldwide) ndi kampani yoziyimilila pa yokha, yosindikizidwa ku England ndi Walesi No. 6394480. Dignity Zambia Limited ndi kampani yomwe anthu aphindulako yosindikizidwa mu ziko la Zambia pa No. 117117